MABUKU MAKUMI AWIRI NDI

MPHAMBU ZISANU

UTHENGA KWA ODWALA

Nkhaniyi ikukamba za machilitso makumi awiri ndi mphambu zisanu. [Idalembedwa ngati chitothozo ndiponso ngati mamkhwala kwa anthu odwala ndicholinga chowafikira ndi kuwafunira kuchira mwa nsanga.]

Chenjezo ndi Chipepeso

Ndondomeko ya machilitsoyi idalembedwa mwachangu kwambiri kuposa zina zonse zomwe ndidalemba [Haşiye] popeza padalibe nthawi yokonza zolakwika ndi kuyiwunikanso, mosiyana ndi zolemba zina zonse ndondomekoyi idangowerengedwa kamodzi kokha mwachangu ngati momwe idalembedweramu. Kutanthuza kuti sizilimundandanda wake. Sindidachione kuti chidali chofunikira kuyang'ananso mosamala zinthu zomwe zidangochitika kwa ine mwa

---

Haşiye: Uthengawu udalembebwa m'maola anayi ndı theka. Ndipo lidasindikizidwa ndi Ruştü, Re'fet, Hüsrev, Saidi.

chilengedwe, powopa kuti zikadatha kuonongeka poziyika mundondomeko ndikukhala nazo chidwi kwambiri. Owerenga makamaka odwala suyenera kukhumudwa ndi kuzimva kulakwiridwa mukafotokozeredwe pazomwe sukugwirizana nazo kapena mau aukali, koma asiye andipemphelere ine.

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

اَلَّذِيْنَ اِذَآ اَصَابَتْهُمْ مُّصِيْبَةٌ قَالُوْٓا اِنَّا لِلّٰهِ وَاِنَّآ
اِلَيْهِ رَاجِعُوْنَ ۞ وَالَّذِىْ هُوَ يُطْعِمُنِىْ وَيَسْقِيْنِ
وَاِذَا مَرِضْتُ فَهُوَ يَشْفِيْنِ

"Ndithudi ife tinachokera kwa Allah ndipo ndi kwa Iye kumene tibwelera"

M'bukuli, tikambirana mwachidule machilitso makumi awiri ndi mphambu zisanu zimene zingapereke chipepeso ndi machilitso opindulitsa kwa odwala ndi amene aphinjika ndi mavuto ambali imodzi ya munthu.

Machilitso Oyamba

O iwe munthu odwala osasangalala! Usakhale odandaula koma khala opilira. Matenda ako simazunzo koma ndi mtundu umodzi wamachilitso.

Moyo umatha ngati mpamba; ngati subala zipatso ndiyekuti ndiwopanda ntchito, ngati sukumana ndi mavuto ndikusamvera umadutsa mwachangu. Kudwala kumapangitsa mpamba wa moyo wako kukolola zochuluka. Koposaposa kudwalako sikumalola moyo wako kudutsa mwachangu, kumateteza ndikutalikitsa moyo kuti uthe kukolola zochuluka. Chidziwitso choti moyo wako umatalikitsidwa kudzera mukudwala ndi mwambi uwu umene umabwerezedwa kawiri kawiri *"Nthawi yamavuto ndiyayitali ndipo nthawi yachisangalalo ndi yochepa kwambiri."*

Machilitso a Chiwiri

O iwe munthu odwala amene supilira! Pilira ndipo uzithokoza. Kudwala kwako kukhoza kusintha mphindi iliyonse ya moyo wako kufanana ndi ola limodzi lakupembedza. Popeza kupembedza kuli m'mitundu iwiri. Kupembedza koyamba nkwabwino komwe ndikodziwikiratu kumene kuli kupempha ndi kuchita ma pemphero asanu a tsiku ndi tsiku. Kupembedza kwachiwiri sikwabwino kumene munthu amachita akakhala ali m'mavuto kapena kudwala. Potengera izi kwa amene amaphinjika, amazindikira kufooka ndi kusowekera kwawo, kenaka amasakasaka *Khalıq-i Rahim* (Mulengi wawo wachifundo chosatha) ndi kupempha thandizo kwa Iye. Amapembedza mokhulupirika ndi mopanda chinyengo. Inde pali kufotokoza kwina komwe kumanena kuti, moyo

umene umadutsa mukudwala umawerengedwa ngati kupembedza kwa munthu okhulupilira ndipo mu nyengoyi iye samadandaula kwa Allah.

Kudakhazikitsidwanso mukafotokozedwe ka anthu amene amanena zoona za chilengedwe kuti: Mphindi imodzi yakudwala kwa anthu opilira ndi wothokoza imafanana ndi ola limodzi lakupembedza ndipo mphindiimodzi yakudwala kwa anthu angwilo imafanana ndi tsiku limodzi lakupembedza. Choncho suyenela kudandaula za kudwala kwako kumene kumasintha mphindi imodzi ya moyo wako kukhala mphindi zikwizikwi zakupembedza ndi kukupezera moyo wautali, choncho ukuyenera kuyamika.

Machilitso a Chitatu

O iwe munthu odwala amene supilira! Zoona zake za amene adabwera pa dziko pano mopitilira amachoka, ndipo wachichepere amakula Kenaka munthu amamwalira. Ndipo kulekanaku ndi umboni wakuti munthu sadabwere pa dziko lino lapansi kudzazikondweretsa yekha kapena kulandira chisangalalo ayi.

Koposaposa munthu ndi opambana ndipo ndiwapamwamba kwambiri, mwazolengedwa zonse, ndiwodalitsidwa potengera ziwalo zomwe iye ali nazo ndi ntchito zake. Ndithudi iye ali ngati mfumu ya zolengedwa zonse za moyo. Kudzera mukuganiza chisangalaro cha m'mbuyo ndi ululu

wa mtsogolo. Ndipo amadutsa m'moyo odandaula, wamavuto kuposa nyama. Izi zikutanthauza kuti munthu sanangobwera pa dziko lino lapansi kudzakhala moyo wabwino ndikudutsa mosavuta ndimosangalalaayi. Koma adapatsidwa mpamba wochuluka ndipo adabwera pa dziko lino lapansi kudzagwira ntchito ndikupanga malonda amoyo wosatha.

Mpamba omwe munthu adapatsidwa ndi nthawi ya moyo wake. Pakadakhala kuti matenda kulibe, moyo wabwino ndi wathanzi zikadayambitsa kusamvera popeza zimaonetsa dziko kukhala losangalatsa ndikuyiwalitsa za moyo ulimkudza. Samafuna kuti imfa ndi manda ziziganiziridwa, zimapangitsa kuti mpamba wa moyo uwonongeredwe pa zinthu zopanda pake. Pamene kudwala kumatsegula maso a munthu ndipo kumanena kwa thupi"si iwe wamuyaya". Ndipo sudasiyidwe ku zolinga zako, uli ndi udindo, siya kudzitukumula kwako, ganiza za amene adakulenga, dziwa kuti udzalowa m'manda, choncho khala okonzeka. Mukuona kumeneku kudwala kuli ngati chidzudzulo ndi malangizo kuti musanyengeke ndi dziko lapansi. Choncho sikoyenera kudandaula pa chimenechi, nkoyenera ndithudi kuthokoza. Ndipo ngati kudwalako sikuoopsya kwambiri, kupilira kukuyenera kukhala njira yochizira matenda.

Machilitso a Chinayi

Munthu odwala odandaula! Sukuyenera kudandaula koma m'malo mwake uziyamika ndikukhala opilira. Popeza thupi ndi ziwalo zako ndi zintchito zake zonsezi sizako. Sudazipange ndiwe kapena kuzigula izo pa msika. Kutanthauza kuti katunduyo ali ndi mwini wake, wina osati iwe, mwini wake amatha kupanga china chilichonse pakatundu wake m'mene akufunira.

Monga m'mene zidafotokozeledwera m'buku lotchedwa "Twenty-sixth Word." Munthu wachuma chochuluka ndi waluso la zosemasema mwachitsanzo; adalemba tchito munthu wosauka ndi cholinga choonetsera ntchito yake yabwino ndi chuma chake chochuluka. M'malo mwa malipiro akanthawi kochepa adamuveka munthu osauka uja zovala zopangidwa ndi golide komanso zolukidwa mwaluso. Amachigwiritsa ntchito pa iye ndi kuchipeleka munjira zambiri pofuna kuonetsa ntchito zake za ukadaulo, amadula chovalachi, kuchisintha, kuchitalikitsa ndiponso kuchifupikitsa. Kodi munthu wa ntchito osaukayi akuyenera kunena kwa munthu uja kuti "Ukundizunza ndi kundikhumudwitsa ndi m'mene wandipangira, kundipangitsa kugwada ndi kuimilira"? Kodi munthu osauka uja akuyenera kumuuza munthu uja kuti akuononga maonekedwe ake abwino podula ndipofupikitsa chovala chake chimene chimamupangitsa kuoneka bwino? Kodi

akhoza kumuuza munthu uja kuti alibe chisoni ndi chilungamo?

O iwe munthu odwala! Ngati m'mene lili fanizoli pofuna kuonetsera chovala cha mthupi lako chimene udavekedwa mwapamwamba ndi ntchito zowala monga diso, khutu, kuganiza ndi mtima opeleka) wake ndi malumikizidwe amayina ake okongola, *Sani-i Dhul jalal* (Mwini matamando) amakupanga kuzungulira munjira zambiri ndi kukusintha mu nyengo zambiri. Ngati m'mene umadziwira za dzina lake la *Ar-Razzaq* (Opeleka) kudzera mu njala, choncho dziwa za dzina lake la *Shafi-i* (Ochiza) kudzera mukudwala kwako popeza kudwala ndi mavuto zimaonetsa ukulu wa mayina ake zitsanzo zochuluka zikupezeka m'mabuku otchedwa *"The Flashes ndi The Rays of Mercy"* Mkatikati mwa mabukuwa muli kukongola kochuluka. Kukadakhala kotheka kuona zomwe zili kuseli kwa matenda amene umawaopa ndi kuwanjenjemera ukadatha kupeza matanthauzo ake ovomelezeka ndi abwino.

Machilitso a Chisanu

O iwe amene wa phinjika ndi matenda, kudzera mu zomwe ndadutsamo! Ndidapanga ganizo pa nthawi imeneyi kwa anthu ena, kudwala ndi chisangalalo chachikulu ndiponso mphatso ya mwini chisoni chosatha. Ngakhale sindimayenera ichi, pazaka zisanu ndi zitatu kapena zinayi za m'mbuyomu ana ochuluka adali kubwera kwa ine

mokhudzana ndi kudwala kwawo, kudzapempha kuti ndi wa pemphelere. Ndidazindikira kuti ena mwa iwo adayamba kuganiza za moyo umene uli mkudza kuposa ana ena achichepele. Sakhala nawo muzochitika za unyamata mpaka amadzisunga kuchokera ku zilakolako za nyama ndi kusamvera. Choncho ndidawaganizira ndipo kenaka ndidawachenjeza kuti kudwala kwawo ndi chisangalalo chachikulu chochokera kwa Allah kudzera m'mayesero akupilira kwawo. Ndidati kwa iwo: M'bale! sindikutsutsana ndi kudwala kwako. Sindikukumvera chisoni komanso chifundo pa kudwala kwako kuti mpaka ndingathe kukupemphelera. Yesela kukhala opilira mpaka kudwala kwako kutakudzutsa kotheratu kufikira kutagwira ntchito yake, Isha allah Khalıq Rahim (Namalenga wa chisoni) adzakupatsanso moyo wa nthanzi m'chifuniro chake. Ndidawauzanso kuti chifukwa cha mavuto a moyo wa thanzi, anzako ena amanyalanyaza ndikusiya kupemphera kasanu pa tsiku, saganizira zam'manda ndipo amamuyiwala Allah wa mphamvu zonse.

Kudzera m'chisangalaro cha kanthawi kochepa cha m'moyo wa pa dziko lino lapansi. Chimagwedeza ndikuononga chisangalaro cha moyo umene uli mkudza kapena kuonongeratu. Pamene chifukwa chakudwala kwako umaona manda amene ungathe kulowamo nthawi iliyonse ndikukhala m'moyo osatha pambuyo pake, ndikuchita moyenelera

choncho kwa iwe kudwala ndimoyo wa thanzi pamene kwa anzako ena, moyo wathanzi ndi kudwala.

Machilitso a Chisanu ndi Chimodzi

O munthu odwala amene umadandaula zakudwala kwako! Ndinena kwa iwe kuti ganiza za moyo wako wa m'mbuyo ndipo kumbukira masiku ako achisangalalo ndi nyengo ya madandaulo ndiyowawitsa ndipo chachidziwikire udzafuula kuti "Oh"kapena "Ah"! kutanthauza kuti mtima ndi lilime lako zidzanena kuti"kalanga ine!" Dziwa ichi, chimene chimakupangitsa kufuula kuti "matamando ndi mayamiko onse apite kwa Allah!" ndikuganizila za ululu ndi mavuto amene ali pa iwe. Zimayambitsa chisangalalo choncho mtima wako umayamika, popeza pa mbuyo pa ululu pali chisangalalo. Pakudutsa kwa maululu ndi mavuto zotsatira za chisangalalo zimatsalira mu uzimu, zimene zimakula chifukwa chakuganiza, zimapangitsa mzimu kuthokoza. Chimene chimakupangitsa iwe kufuula kuti "Kalanga ine!" ndi nthawi ya chisangalaro ndi ya chikondwelero imene udadutsamo, imene pakudutsa kwake imasiya mavuto a ululu mu uzimu wako. Pamene ukuganiza za ululu umakhala ukuyendayendanso umene umapangitsa kuganiza zolakwika za m'mbuyo ndi chisoni cha mtsogolo kukondwelera chisangalaro chosavomelezeka kwa tsiku limodzi, nthawi zina kumapangitsa mzimu

wako kuvutika kwa zaka zochuluka. Ndipo ululu wamatenda umene umachitika kwa masiku ochepa umabweretsa masiku ochuluka a chisangalaro. Popeza chimayambitsa mavuto a chaka chonse. Ku uzimu ndi ululu wakudwala wa masiku ochepa umabweretsa chisangalalo cha masiku ochuluka ndi mphoto poonjezera pa chisangalalo, pakuomboledwa ndi pakudutsa kwake. Ganiza zazotsatira zakudwala kosakhalitsako kumene wa phinjidwa nako ndi ubwino wake omwe uli nawo nena kuti "Zonse zimachokera kwa Allah! Izinso zidzatha!" ndikumuyamika m'malo momangodandaula.

Machilitso a Chisanu ndi Chimodzi **(Haşiye)**

O m'bale amene umaganiza za zisangalalo za pa dziko lapansi ndi kumadandaula pa kudwala kwako! Ngati dziko lapansi lino likanakhala la muyaya, ngati moyo wathu ukadakhala opanda imfa ndipo ngati imfa ndi mphepo yokulekanitsa sizinauzilidwe ndipo ngati kukadakhala kuti muuzimu wathu mulibe nyengo zowawitsa za m'mavuto ndi tsogolo lovuta, ndikadakumvera chisoni iwe. Koma popeza tsiku lina dziko lidzatisiya ife ndi kutseka makutu

Haşiye: Uthengawu udangochitika kwa ine mwa chilengedwe ndipo machilitso awiri aphatikizidwa mu machilitso a chisanu ndi chimodzi. Tazisiya, kuopa kuti zingaononge mwa chilengedwe. Indedi sitidawasinthe poganizira pakhoza kukhala kusamvetsetseka mu izo.

ake pakulira kwathu. Tikuyenera kusiya kulikonda pakudzera m'machenjezo akudwalaku. Dzikoli lisadatisiye, ife tikuyenera kulisiya m'mitima mwathu. Indedi kudwala kukupereka chenjezo kwa ife kuti, thupi lako siridapangidwe ndi miyala kapena zitsulo koma zinthu zamitundu mitundu zimene chiyambire sizidagwirepo ntchito yake mosiyana. Siya kudzitukumula kwako, vomereza kufooka kwako, zindikira muyang'aniri wako, zindikira udindo wako, ndikudziwa chimene unabwelera pa dziko lapansi pano! Mwa chinsisi ichi chimaululika m'mitima mwathu. Koposaposa, popeza zisangalalo ndi zikondwelero za dziko lino sizipitilira, makamaka ngati zili zosaloledwa zonsezo ndi zosakhalitsa, zodzadza ndi ululu ndinso za uchimo. Usalire chifukwa chakudwala, popeza wataya zisangalo zonse koma m'malo mwake, ganiza zakupembedza ndi mphoto zake za m'moyo uli mkudza zimene zimapezeka mukudwala ndipo yesera kupeza chisangalalo mukudwala kwako.

Machilitso a Chisanu ndi Chiwiri

O iwe munthu odwala amene wataya chisangalalo chamoyo wako wathanzi! Kudwala kwako sikumaononga chisangalalo chazabwino koma kumabweretsa chisangalalo ndipo chimaonjezereka. Ngati china chake chikupitilira sichikhala ndi zotsatira zake. Ngakhale anthu eni eni amati

اِنَّمَا الْاَشْـيَاءُ تُعْرَفُ بِاَضْدَادِهَا

"Zinthu zimadziwika kudzera muzotsutsana nazo." Mwachitsanzo; ngati kukadakhala popanda m'dima kuwala sikukadadziwika ndipo sikukadabweretsa chisangalaro. Kukadapanda kukhala kuzizira, kutentha sikukadamvekanso, kukadakhala kopanda njala chakudya sichikadabweretsa chisangalalo. Kukadakhala kuti ludzu kulibe, sikukadakhalanso chisangalalo chakumwa madzi. Kukadakhala kopanda matenda, ndiye kuti ubwino wa moyo wathanzi sukadakhalaponso.

Fatiri Hakim (Allah wa nzeru zonse) adampanga munthu ndizinthu zoonadi, zochuluka ndi ntchito zake, mpaka amazigwiritsa ntchito ndi kuzindikira mitundu yochuluka yazisangalalo m'dziko lapansi. Zimaonetsa kuti Allah amafuna kumupanga munthu kuti adziwe za mtundu uliwonse wa zabwino zake, kumuonetsa ndi kumpangitsa iye kuti akhale othokoza. Popeza izi zili chomwechi, Allah amapereka matenda ndi kuvutika, chimodzimodzinso ngati m'mene amampatsira moyo wathanzi ndi kukhala wangwiro. Nditakufunsani "Ngati simudavutikepo ndi matendawa m'mutu mwanu kapena mdzanja lanu kapenanso m'mimba mwanu, kodi mukuganizira zachisangalalo ndi chimwemwe cha zabwino za moyo wathanzi wa m'mutu mwanu, dzanja ndi

m'mimba mwanu ndi kuthokoza?" Chachidziwikire simukadaganiza ngakhale za ichi. Mosaganizira ukadaononga moyo wathanziwo pakusamvera ngakhale kuononga.

Machilitso a Chisanu ndi Chitatu

O iwe munthu odwala amene umaganiza zamoyo ulinkudza! Kudwala kumachotsa litsiro la machimo ngati sopo ndikuyeretsa. Zikupezeka mu Hadith ina yonena kuti *"Matenda amadza kamba ka machimo"* ndipo mu Hadith ina imanena kuti *"Monga m'mene zipatso zakupsya zimagwera m'mitengo yake ikagwedezeka, chimodzimodzinso machimo amunthu okhulupilira amachoka pakugwedezeka kwake ndi matenda."*

Machimo ndi matenda owopsya omwe amakhudza moyo osatha ndipo moyo wa dziko lino lapansi machimo ndi matenda a mu mtima, m'maganizo ndi mu uzimu. Ngati ukhala opilira ndi osadandaula, udzapulumutsidwa kumatenda akanthawi kochepawa kuchokera kumatenda ochuluka okhalitsa. Ngati suganiza zamachimo ako ngakhale kudziwa za m'moyo umene uli nkudza kapena kudziwa Allah, udzavutika ndi matenda, choncho kuchita nawo mantha ndikoipa kwambiri kuposa matenda ang'ono amene ulinawowo. Lira pachimenechi, popeza zachilengedwe zonse za m'dziko lino zidalumikizidwa ku mitima, thupi ndi mzimu wako. Nthawi zonse zolumikizidwazi zimalekanitsidwa ndi imfa ndikutsegula mabala

akuluakulu. Makamaka pakuti sudziwa zamoyo umene ulinkudza ndi kuganiza za imfa ndi mathero a zonse ndiponso chinthu choopsya choncho matenda ako amakula.

Kutanthauza kuti chinthu choyamba chimene ukuyenera kuchita ndi kusakasaka machilitso achikhulupiliro amene ali ngati machilitso amatenda ochuluka amene aphinja mabala ndi odwala, zinthu zako zikuluzikulu; Nkoyenera kukhonza chikhulupiliro chako. Njira yaifupi yopezera machilitsowa ndikuzindikira *Qadir Dhul jalal* (mphamvu ndi chifundo cha wamphamvu zonse) ndi kusowekera kwako, zimakuonetsa kwa chotchinga cha kusamvera kwako. Zimalipilidwa ndi kudwala kwako kwa thupi.

Indedi munthu amene sazindikira Allah amaphinjika ndi dziko lapansi lodzadza ndi mavuto. Pamene dziko la munthu amene amazindikira za Allah ali odzadzidwa ndikuwala komanso chikhulupiliro cha uzimu. Amazindikira za izi molingana ndikukula kwa chikhulupirilo chake. Mavuto odza kamba kakudwala kwa thupi kumachotsa chimwemwe cha mu mtima. M'machilitso ndi chisangalalo chimene chimakwera kuchokera m'chikhulupilirochi. Motero mavuto saonekanso.

Machilitso a Chisanu ndi Chinayi

O iwe munthu odwala amene umamudziwa Namalenga wako! Kudwala kumabweretsa ululu,

mantha ndi kukhumudwa chifukwa nthawi zina kumadzetsa imfa. Kwa anthu osalabadila ndi osamvera amaona ngati imfa ndi chinthu chochititsa mantha. Kudwala kumene kungabweretse imfa kumayambitsa mantha ndi kunjenjemela. Choncho dziwa.

Choyambilira; Kukhulupilira kuti ola lokhazikitsidwa ndilokhazikika ndipo silimasintha. Amene akulira pambali pa kudwala modandaula ndi amene ali m'moyo wangwiro onse amamwalira. Pamene odwala odandaula nthawi zina amachizidwa ndikukhala ndi moyo.

Chachiwiri; Imfa siyochititsa mantha ngati m'mene imaonekera. Kudzera mkuwala kothekera kwa bukhu la nzeru zonse la Qur'an ndi m'magawo ambiri a Risale-i Nur tatsimikiza kothelatu kuti kwa okhulupilira imfa ndikuchotsedwa muntchito zolemetsa za m'moyo uno. Kwa iwo imfa ndi nthawi yopuma ku kupembedza kumene ndi lamulo ndi kukonzekera chiweruzo cha m'dziko lino lapansi ndi njiranso yokumanirana ndi abale ndi anzako amene adachoka kale pa dziko pano. Njira yolowera kumalo enieni kumene adachokera ndi kuchisangalalo chachikulu. Kuli ngati kuitanidwa ku minda yaku paradiso kuchokera mu m'dima wa dziko lino. Ndinthawi imene amalandila malipiro awo kwa *Khalıq Rahim* (Namalenga wa chisoni chosatha) pakutumikira Iye. Popeza tanthauzo lenileni la imfa ndi limeneli, choncho

isamatengedwenso ngati yochititsa mantha, koma ngati chiyambi ku chifundo ndi chisangalalo.

Nthawi zambiri anthu amene amaopa Allah imfa siimakhala yoopsya kwa iwo chifukwa amayembekezera kulandila zabwino zoonjezera pochita ntchito zabwino zochuluka ndi ntchito za moyo wopitilira. Indedi kwa anthu achikhulupiliro, imfa ndi khomo la chifundo. Pamene kwa anthu osochera, imfa ndi dzenje la m'dima wa muyaya.

Machilitso a Chikhumi

O iwe odwala amene umangodandaula! Umadandaula kwambiri za matenda ako ndipo kudandaula kumaonjezera matendawo. Ngati ukufuna kuti kudwala kwako kusakhale koopsya, yesera kusiya kudandaula. Ndipo ganiza za mphoto ya kudwala kwako ndi malipiro ake ndipo kuti kudzatha mosakhalitsa, kudzachotsa nkhawa zonse ndi kuchizilatu matenda.

Zoona kudandaula kumaonjezela matenda popeza kumayambitsa matenda a mtima pambali pa matenda enieniwo; matenda enieni amapitilira kudzera mu kudandaula. Ngati kudandaula kutha kudzera mukugonjera, kuvomeleza ndi mtima ndi kuganiza mwa nzeru za matendawo kenaka gawo lalikulu la matenda limachoka, sakhalanso owopsya ngati kale, kuwopsya kwake kumachepa ndipo kenaka kumachoka. Nthawi zina matenda enieni ang'ono amakula kamba kakukhumudwa. Ngati

kukhumudwako kutha, gawo lalikulu la matenda limachoka. Kudandaula kumakulitsa matenda ndipo kumasutsananso ndi Allah komanso kudzudzula chifundo chake ndi kumudandaula *Khaliq Rahim* (Namalenga wa chisoni.) Pa chifukwa chimenechi, munthu amene amadandaula savomelezedwa ndipo kudwala kwake kumaonjezeleka mosiyana ndi malingaliro ake. Indedi monga kuthokoza kumaonjezera zabwino, chonchonso kudandaula kumaonjezera matenda ndi mavuto.

Kuonjezera apa, kudandaula pakokha ndi matenda. Mankhwala ake ndi kuzindikira za matenda ndi cholinga chake. Popeza pano waphunzira za cholinga ndi phindu la kudwala. Choncho, zigwilitse ntchito pothetsa nkhawa zako ndi kupeza chithandizo. Nena kuti "Ah!" m'malo mwa "Oh!"ndipo *"Alhamdulillah ala kuli hal"* pachina chilichonse m'malo momadandaula.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Imodzi

O iwe m'bale wanga odwala amene umalephera kupilira! Ngakhale matenda amayambitsa mavuto ansangansanga. Matenda ako, kuchokera m'mbuyo kufikira pano amapeleka chisangalaro cha uzimu kudzera m'mphoto yobwera kamba kakupilira nawo kuyambira lero kumka mtsogolo, ngakhalenso kuchokera muola lino, matenda palibe ndipo cholengedwa chilichonse sichivutikanso ndi ululu. Ndipo ngati palibe ululu sipangakhalenso madandaulo. Umalephera kupilira chifukwa

umaganiza zinthu molakwika. Popeza matenda akuthupi alero ndi ululu wake zachoka. Zomwe zatsala ndi mphoto zake ndiponso chisangalaro pakuthakwake.Popezaichichimakupatsaphindundi chisangalaro, choncho kuganiza za masiku ambuyo, kumadandaula ndi kusapilira ndikuzelezeka chabe, masiku amtsogolo asanafike. Kuganiza za iwo ndi kuganizira za tsiku lomwe palibe, matenda amene palibe, nkhawa zimene palibe, kuonetsa kusapilira ndi kuzipanga kukhalapo, kumeneku ndikutani ngati sikuzelezeka?

Ngati ola la mbuyo lidali la matenda limabweretsa chimwemwe ndipo popeza nthawi yabwera ku ola latsopano silinapezeke ndipo kuti matenda ndi nkhawa sizipezeka. Osataya mphamvu za kupilira zomwe zidapatsidwa kwa iwe ndi Janab-i Haqq (Allah wa mphamvu zonse) kumanja ndi kumanzere kwako, koma uzionetsa mphamvuzi pa ululu wa ola lino. Nena *"Ya Swabur!"*,"O Wakupilira konse!"

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Ziwiri

O munthu odwala amene sungathe kuchita mapemphero ako ndikukhala odandaula ndi kusasangalala! Zindikira kuti zinanenedwa mu Hadith; *"Anthu owopa Allah amene chifukwa chakudwala sangathe kuchita mapemphero awo atsiku ndi tsiku, amalandira mphoto yake yofanana ndi izo."* Ngati munthu odwala akuchita mapemphero ake m'mene angakwanilitsire

mopilira ndi kudalira mwa Allah, matenda ake amakhala ngati Sunnat m'malo mwake. Mu nthawi ya matenda oopsya ndipo kupembedza kwake kumakhala kwa choonadi.

Kuonjezera apa, matenda amapangitsa munthu kumvetsetsa za kufooka ndi kusowekera kwake, komwe kumamupangitsa munthu kuyamba kupembedza kudzera pakamwa, mukufooka ndiponso mukusowekera kwake. *Janab-i Haqq* Allah wamphamvu zonse adapereka kwa munthu kusowekera kwakukulu ndi kufooka kwambiri kuti akatero akhala akusakasaka chithandizo pamalo ake oyera ndi kuchipeza Kenaka ndikuchita dua.

قُلْ مَا يَعْبَؤُا بِكُمْ رَبِّي لَوْلَا دُعَاؤُكُمْ

Mogwilizana ndi tanthauzo la vesili nena kuti; "Mbuye wako sakadakhuzika nawe pakadapanda mapemphero ako." Kutanthauza kuti *"Ndikufunika kwanji komwe uli nako ngati supemphera ndikuchita dua?"*. Molingana ndi izi, pemphero lenileni ndikuchita dua, chifukwa chimene munthu adalengedwera chakupambana kwake. Popeza matenda ndi chiyambi chimodzi cha ichi, kuchokera mukuona kumeneku sakuyenera kudandaulidwa koma m'malo mwake muyamike Allah, uwu ndı mpope wa mapemphero umene matenda amatsegula, sukuyenera kusekedwa pokhalanso ndi moyo wa thanzi.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zitatu

O munthu osasangalala amene umadandaula ukadwala! Kwa anthu ena matenda ndichuma chochuluka, mphatso yaikulu yopambana. Munthu odwala aliyense akhoza kuganiza za matenda ake munjira iyi.

Nthawi yokhazikitsidwa siikudziwika, pofuna kuombola munthu kuchokera mu kubalalika ndi mukusamvera kwenikweni, ndikumugwira pakati pa chiyembekezo ndi mantha choncho ndikusunga moyo uno ndi moyo uli nkudza. Mu nzeru zake, *Janab-i Haqq* (Allah wa mphamvu zonse) anabisa ola lokhazikitsidwa limene limatha kubwera pa nthawi ina iliyonse. Ngati limuyika munthu mukusamvera, limayambitsa kudandaula ndi kuononga moyo osatha. Matenda pena amachotsa kusamvera, amamupangitsa munthu kuganiza za moyo uli nkudza, amakumbutsa za imfa choncho munthu amatha kukonzekera pa iye yekha. Matenda ena ndi aphindu kwa munthu, amakhala opambana m'masiku makumi awiri kumene sakadatha kukwaniritsidwa mu zaka makumi awiri.

Mwachitsanzo; mwa anzanga, padali achinyamata awiri, Allah awachitire chifundo. M'modzi adali *Sabri*, ochokela m'mudzi wa *Ilema*, ndi wina *Verzirzade Mustafa* ochokela ku *Islamkoy*. Ndimazindikira modabwa kuti ngakhale awiriwa samatha kulemba adali mgulu la anthu odziwika kwambiri potengela choonadi ndi kutumikila mwa

chikhulupiliro. Sindinadziwe m'mene izi zidaliri chomwechi. Atamwalira onsewa ndidamvetsetsa kuti onse adadwaladi matenda oopsya. Kudzera muchiongoko cha matendawo, mosiyana ndi achinyamata ena onyalanyaza amene adasiya mapemphero olamulidwa, adachita mantha ndi Allah kenaka adayamba kumutumikira mwapamwamba ndikupeza zabwino m'moyo umene uli nkudza. M'chifuniro cha Allah, kukhumudwa ndimatenda, kwa zaka ziwiri kudawapangitsa kupeza chisangalalo chazaka ma miliyoni za moyo osatha umene uli mkudza.

Tsopano ndamvetsetsa kuti mapemphero amene ndimapanga amoyo wawo wathanzi ndi matembelelo am'dziko lino. Mchifuniro cha Allah, mapemphero anga adavomelezedwa pakuchita bwino kwawo m'moyo umene uli nkudza.

Ndiye kuti motengera chikhulupiliro changa, awiriwa adapeza phindu lofanana limene lingathe kupezedwa kudzera m'zaka khumi ali ndi taq'wa (kuopa Allah.) **(Haşiye)** Ngati anthu ena achichepere, amadalira unyamata wawo wathanzi ndi kuziponya okha mukusamvera ndi m'makhalidwe onyasa ndi kuwatsatira, kenaka imfa ndikuwatenga pa maso pa

Haşiye: Tanthauzo la Hadith lili motere; Ngati munthu angayime pa maso pa Allah ndipo sangathe kufika kumaloko kudzera mu zıntchito za bwino, Allah amampatsa matenda ndi mavuto oterowo amakhala ngati akudwala mpaka pamene atachira.

zonyasa za machimo awo, m'manda awo akadakhala malo ogona zinkhanira ndi njoka m'malo mwa chuma chowalacho. Popeza m'matenda muli phindu limeneli, choncho asamadandaulidwe koma kuwapilira ndi kudalira mwa Allah. Ndithudi thokoza Allah ndipo ukhale ndichikhulupiliro mu chifundo chake.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zinayi

O munthu odwala amene maso ako akhudzidwa ndi matenda! Ukadadziwa zakuwala ndi diso la uzimu zikupezeka pansi pa matenda amene atchinga maso a anthu okhulupilira, ukadafuula kuti *"Mayamiko ochuluka apite kwa **Rabbi Rahim** (Nsungi wachisoni)!"* Ndifotokoza ichi potengera ndi zomwe zidachitika. Zili motere:

Nthawi ina azakhali a Sulaimana ochokera ku *Barla* amene adandisunga ine kwa zaka zisanu ndi zitatu mokhulupirika ndi mwa chifuniro, tsiku lina adasiya kuona. Chifukwa chondifunira zabwino, zimene zidali zochuluka kuposa m'mene ndimayenelera, mayi wa ngwiroyu adandigwira ndikupita nane pakhomo la nzikiti kundipempha kuti ndimupemphelere kuti ayambenso kuona. Choncho ndinampanga mayi wa ngwiroyu kukhala m'mapemphero anga ndikumupempha Allah wamphamvu zonse Kenaka ndidapemphera. *"Oh Allah bwenzelani kuona kwa mayiyu potengera ndi ungwilo wake"* patapita masiku awiri dotolo wa zamaso ochokera ku Burden adabwera

ndikumuchotsa chimene chimamuvuta mmaso mwake Kenaka adayambaso kuona. Patatha masiku makumi anayi mayi uja adasiyanso kuona ndidakhumudwa kwambiri ndipo ndidamupemphelera molimbika. M'chifuniro cha Allah pemphero lidavomelezeka m'moyo uli nkudza. Mwa njira ina pemphero langali likadakhala lolakwika kwa iye popeza masiku makumi anayi adatsala mpaka imfa yake. Patapita masiku makumi anayi adamwalira- Allah amuchitire chifundo.

Kutanthauza kuti, mayi uja adakhala wachisoni pa minda ya Barla ndi diso lake laukalamba m'malo mwake adapindula m'manda mwake poyang'ana minda yaku paradiso kwa masiku zikwi makumi anayi. Popeza chikhulupiliro chake chinali cholimba ndipo anali wangwiro kotheratu.

Indedi ngati munthu okhulupilira asiya kuona kwake nalowa m'manda akanali wa khungu, mogwirizana ndi ntchito zake akhonza kuona dziko lowala kwakukulu kuposa akufa ena onse amene ali m'manda. Monga momwe timaonera zinthu zochuluka m'dziko lino zimene akhungu okhulupilira samatha kuziona. Ngati kusaonako kulekana ndi chikhulupiliro, amaona kwambiri kuposa akufa ena m'manda mwawo. Amalandira minda yaku paradiso ndikumaonera ngati kanema kudzera m'makina amphamvu kwambiri mogwilizana ndi ntchito zawo.

Kutanthauza kuti kudzera m'mayamiko ndi kupilira ukhoza kupeza pansi pa chotchinga, maso ako amene ndi odzadza ndi kuwala, omwenso angakupangitse kuona paradiso pamwamba pa mitambo ndi pansi pa nthaka. Chimene chidzachotsa chotchinga mmaso mwako, dotolo amene adzapanga diso lako kuti liwone ndi buku la nzeru zonse lomwe ndi Qur'an.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zisanu

O munthu odwala amene ukubuula ndi kumadandaula! Usayang'ane zinthu zakunja zamatenda ndi kubuula koma ganiza tanthauzo lake ndi kukhala osangalala, ngati tanthauzo la matenda a bwino. *Khalıq Rahim* (Allah wachisoni chonse) sadakapereka matenda kwa akapolo ake omwe amawakonda. Ndipo pali Hadith

اَشَدُّ النَّاسِ بَلَاءً اَلْاَنْبِيَاءُ ثُمَّ الْاَوْلِيَاءُ
اَلْاَمْثَلُ فَالْاَمْثَلُ

yomwe tanthauzo lake ndi *"Onse amene amaphinjidwa ndimatenda kapena mayeselo akulu ndi aneneri, kenaka anthu oyera mtima ndi ena ngati iwowo."* Kutanthauza kuti; anthu amene amaphinjidwa ndimavuto kapena zikhomo ndi opambana kwambiri ndiponso ndi angwiro. Ngati m'mene *Hazret Ayyub* (Alayhi Ssalam) ndi aneneri ena, anthu oyera ntima ndi ochita ntchito zabwino

adawatenga matenda awo amene adavutika nawo ngati kupembedza kwa bwino komanso ngati mphoto yochokera kwa mwini chisoni ndipo amamuyamika moleza ntima. Amawona ngati opaleshoni yochitidwa ndi chifundo cha Khaliq Rahim.

O iwe amene umalira ndi kudandaula! Ngati ukufuna kukhalamo m'chombo chowalachi peleka mayamiko ako moleza mtima. Ngati udandaula suzavomelezedwa udzagwela m'mayenje a anthu osochela ndi kuyenda mu njira ya m'dima. Inde pali matenda ena ngati akufikitsa ku imfa, ali ngati anthu omwalira ofera chipembedzo ndipo amafanana ndi anthu oyera mtima. Mwachitsanzo; anthu amene amamwalira ndi matenda ngati mwana obadwa kumene ndi ululu wa m'mimba **(Haşiye)** kapena kufera m'madzi ndi moto kapena mulili oopsya amakhala ngati anthu amene adafera chipembedzo. Palinso matenda ena ochuluka odalitsika amene munthu ngati amwalira nawo amampangitsa kukhala oyera ntima. Monganso matenda amachepetsa chikondi cha padziko lapansi ndi kugwilizanitsa, amawaletsa kulekana kuchokera ku dziko lino kudzera mu imfa, zomwe zili zomvetsa chisoni ndizopweteka m'dziko ndipo nthawi zina matenda amapangitsa kuwafunafuna.

Haşiye: Nthawi ımene anthu ofera chipembedzo angapeze kudzera mu matenda amakhala ali chigonere m'masiku makumi anayi.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zisanu ndi Chimodzi

O iwe munthu odwala amene umadandaula podera nkhawa za matenda ako! Matenda amakumbutsa za ulemu ndi chisoni zimene zili zofunika kwambiri ndi zabwino m'moyo wa munthu wa makono. Popeza amamuteteza munthu kuchokera mukudzikundikira kumene kumampititsa kumoyo osakhala ndi anzake ndi kukhala opanda chisoni. Potengera tanthauzo lavesili

اِنَّ الْاِنْسَانَ لَيَطْغٰٓى اَنْ رَّاٰهُ اسْتَغْنٰى

"Ndithudi munthu amaphwanya magoli choncho amaziona ngati okwanira pa iye yekha." Mzimu olamulira zoipa umene umapangitsa kuzindikira chifukwa cha moyo wathanzi ndi kuchita bwino, sulabada zakupeleka ulemu kwa abale ake amene akuyenera ulemuwo munjira zambiri. Ndiponso sumvera chisoni anthu odwala ndi anthu omwe akhudzika ndi ngozi. Ngakhale kuti anthuwo akuyenera chifundo ndi chisoni pamene akudwala amamvetsetsa zakupanda mphamvu kwake ndi zosowa zake ndipo amalemekeza abale ake. Amalemekeza abale ake okhulupilira amene amamuchezela ndi kumuthandiza. Amavela anthu ena chifundo kuchokera pansi pa ntima wake ndi kuchitira chisoni amene akumana ndi ngozi. Chimenechi ndi chimodzi chofunikira kwambiri

m'chisilamu. Potengera iye ndi anthu amene amawamvera chisoni chenicheni ndi kuwachitira chifundo. Amapanga zomwe angakwanitse kuwathandiza ndi kuwapemphelera ndiponso kuwafuna m'mene alili, imene ndi *Sunnat* motengera sharia ndipo amalandila mphoto.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zisanu ndi Ziwiri

O munthu odwala amene umadandaula kuti sugwila ntchito zabwino chifukwa chamatenda! Yamika ndimatenda amene amakutsegulira khomo la ntchito zabwino zenizeni. Moonjezera ndikupeza mphoto kawirikawiri kwa munthu odwala ndiponso kwa amene akumuyang'anira. M'chifuniro cha Allah, matenda ndiwofunika kwambiri omwe amapangitsa kuti mapemphero avomelezedwe. Indedi pali mphoto yofunika kwambiri kwa okhulupilira amene amayang'anira munthu odwala. Kusamalira za moyo wawo wa nthanzi ndi kuzonda odwala salipidwa kalikonse koma ndi sunnat ndiponso malipiro amachimo. Pali Hadith yomwe imanena kuti *"Kulandira mapemphero amunthu odwala popeza mapempherowo ndiovomerezeka."*

Kuyang'anira munthu odwala makamamaka pachibale kapenanso makolo ndikupembedza kofunikira kumene kumabweretsa mphoto yofunika kwambiri. Kusangalatsa mtima wa munthu odwala ndi kumutonthoza kuli ngati kupeleka *swadaka* (chopereka cha ulele). Wamwayi ndi munthu

amene amasangalatsa mitima yokhudzidwa ya bambo ndi mayi pa nthawi ya kudwala kwao ndi kulandira mapemphero awo. Ngakhalenso Angelo amasangalala ndi kufuula kuti; *Mashallah! Barakallah!* Makanda ndi abwino chifukwa ndi amene amapereka ulemu ndi kumva chisoni pa nthawi ya kudwala kwa makolo awo. Makolo awo amaonetsa umunthu weniweni, popeza ndi amene akuyenera kulandira ulemu koposa m'moyo uno. Indedi, muli zisangalaro pa nthawi ya kudwala, zimenezi zimakwera kuchokera ku chifundo ndi chisoni cha amene chawazungulira. Ndipo amakhala osangalala ndi kuvomeleza za matenda awo ndipo izi zimathetsa ululu wa kudwala kwawo. Kuvomelezedwa kwa mapemphero amunthu odwala ndi chinthu chofunika kwambiri. Poti zaka makumi atatu kapena anayi za m'mbuyo, ine mwini ndidapemphera kuti ndichilitsidwe kumatenda a Lumbago omwe ndimadwala koma ndidamvetsetsa kuti matendawa adapelekedwa chifukwa cha pemphero. Popeza pemphero silingachotsedwe ndipemphero. Kutanthauza kuti; Pemphero silingazichotse lokha, ndidamvetsetsanso kuti zotsatira za mapemphero zimakhala za moyo osatha **(Haşiye)** ndipo ndi mtundu wakupembedza. Poti kudzera m'matenda munthu amamvetsetsa

---

Hâşiye: Eya pamene matenda ena ndichifukwa chakupezeka kwa pemphero, ngati pemphero ndi chiyambi cha kusapezeka kwa matenda, kupezeka kwa

⟶

zakusowekera kwake ndipo amafunafuna thandizo pamalo oyera choncho ngakhale kwa zaka makumi atatu, zimene ndidakhala ndikuchita mapemphero kuti ndichilitsidwe mpaka pano mapemphero anga sanavomelezedwe komabe sindidagwe mphwayi.

Popeza matenda ndi nthawi yochita mapemphero. Kuchilitsidwa sichotsatira chakupemphera. Koma ngati *Janab-i Haqq Rahim* (Allah wanzeru ndi chisoni chonse) amapereka machiritso, Iye amapeleka mwa chisomo chachikulu. Kuonjezela apa ngati mapemphero sayankhidwa monga m'mene tikufunira, sitikuyenera kunena kuti sadavomelezedwe.

Allah wanzeru zonse amadziwa bwino kuposa ife: Amatipatsa ife chilichonse chimene chingatisangalatse. Nthawi zina zisangalaro zathu zimapititsa mapemphero athu a m'dziko lino lapansi ku moyo umene uli nkudza ndi kuwavomera munjira imeneyi. Mchochitika chilichonse, pemphero limene likufunika chifukwa cha matenda ndikukwera kuchokera mukufooka kwathu, kusowekera, kupondelezedwa ndi kufunika munthawi yake ndi lapafupi kwambiri kuvomelezedwa. Matenda amapangitsa pemphero kukhala loonadi. Anthu amene akudwala ndi

---

pemphero chikadakhala chifukwa cha kusapezeka kwake ndipo silikadakhala vuto.

okhulupilira amene akuyang'anira odwala atengelepo mwayi pa pempheroli.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zisanu ndi Zitatu

O munthu odwala amene umasiya kuthokoza ndi kuyamba kumadandaula! Dandaulo limachokera mu ubwino ndipo palibe chabwino chako chilichonse chimene chatayika kuti uzidandaula. Indedi, pali mayamiko ambirimbiri amene ali okakamiza komanso amene ali abwino pa iwe ndipo izi sungachite popanda *Janab-i Haqq* kukupasa zabwino umadandaula pofuna zabwino munjira yosayenera. Sungayang'ane kupambana pa iwe ngati m'mene anthu a moyo wathanzi amadandaulira. Koma umalamulidwa kuyang'ana kwa odwala amene powona zamoyo wake wathanzi ndi otsika kuposa iwe mwini, ndipo uyenera kuthokoza. Ngati dzanja lako lavulala yang'ana manja awo amene avulala koopsya. Ngati uli ndi diso limodzi yang'ana amene ali osaona amene alibe maso onse awiri ndipo uzimuyamika Allah.

Mwachidziwikire palibe angamayang'ane zakupambana kwa iye potengera pazisangalalo ndi madandaulo. Mokhudzana ndi mavuto aliyense akuyenera kuyang'ana ali pamwamba pawo choncho akuyenera kupereka mayamiko. Izi zafotokozedwa m'malo ambiri mu *Risale-i Nur* muzitsanzo; Chidule chake cha ichi chili motere; Munthu wina adatenga munthu ovutika kwambiri

ndikupita naye pamwamba pa nsanja. Pasitepe iliyonse amamupatsa mphatso yosiyana ndi chosangalatsa. Pamwamba penipeni adamupatsa mphatso yayikulu kwambiri. Ngakhale amafuna mayamiko ndi mathokozo pa mphatso zonse zosiyanazi munthu ovutikayo adaiwala za mphatso zimene adapatsidwa pa gawo lililonse, ndikuziganiziranso mphatso zija kukhala zosafunikira kwa iye. Posayamika adayang'ana pamwamba nayamba kudandaula ndikunena kuti "Ikanakhala kuti nsanjayo idali yayitali ndikadatha kukwerabe, ndichifukwa chiyani sili yayitali ngati phiri lili uko, kapena nsanja inayo?" Ngati akuyamba kudandaula chonchi, ndikusayamika kwa mtundu wanji kumene kungakhalepo? Ndikulakwa kwanji?

Munjira yomweyi munthu sadachokere kuchina chilichonse osati ngati nthanthwe, mtengo kapenanso nyama ayi koma ngati munthu komanso Muslimu. Nthawi zambiri amakhala m'moyo wathanzi ndipo amafuna zisangalalo za pamwamba posatengera kudandaula ndi kuonetsa kusapilira kwake. Popeza sali oyenera kukhalanso muzisangalalo zina popeza adazitaya kudzera muchisankho cholakwika ndi kuzigwilitsa ntchito molakwika ndikutinso sadazipeze podzudzula *Rububiyeti Ilahi* (za ulamuliro waukulu) ponena kuti "Ndichiyani chomwe ndachita kuti izi zichitike kwa ine? Ndimatenda am'maganizo komanso mu uzimu ovuta kwambiri kuposa apathupi. Ngati kumenya ndi nkono ovulala, kudandaula

kumapangitsa matenda kufika povuta kwambiri. Munthu wanzeru ndi amene amazipereka ndi kudekha motengera tanthauzo la vesili

لِكُلِّ مُصِيبَةٍ اِنَّا لِلّٰهِ وَاِنَّآ اِلَيْهِ رَاجِعُونَ

"Kwa onse amene amagwera m'mavuto amanena kuti", " Ndithudi ife tidachokera kwa Allah ndipo ndi kwa Iye kumene tibwelera"

Choncho kuti matenda amalize ntchito yake kenaka achoke.

Machilitso a Chikhumi ndi Mphambu Zisanu ndi Zinayi

Ngati chikumbutso cha opereka wa muyaya, *Jamil Dhul Jalal* "mayina okongola kwambiri" amaonetsa kukongola konse kwa mayina otamandika kuti ndi okongola. Pakuti pa zolengedwa, moyo ndiosamvetsetseka, okongola kwambiri ndi kalilole omvetsetseka kwambiri wa wakupereka kwa muyaya, Allah. Kalilole owonetsa kukongola amasanduka kukhala okongola. Kalilole amene amaonetsa makhalidwe abwino ndi kukongola amasanduka okongola. Monga ngati m'mene chilichonse chimachitika pa kalilole ndi kukongola uku ndi chabwino komanso ndi chokongola, chilichonse choopsya m'moyo zoona zake ndi chabwino popeza chimaonetsa kukongola muchisangalatso cha mayina okongola koposa amene ali abwino ndiponso okongola.

Moyo umakhala kalilole opelewera ngati udutsa mu zinthu zosakhala bwino m'moyo weniweni wathanzi ndi wabwino. Ndithudi mwanjira imodzi amaganiza zakusapezeka, kusakhalapo ndi kuyambitsa mkwiyo. Zimachepetsa kufunika kwa moyo ndi kusintha zosangalatsa m'moyo kukhala nkhawa. Popeza poganiza kuti udzatha nthawi yake mofulumira, mukunyasidwa munthu amaziponyela yekha m'mbuyo kapena muzisangalalo. Ngati chilango chakundende, amasanduka otsutsa moyo wake wapamwamba ndipo amafuna kupha ndikuwupangitsa kutha mwansanga. Koma ukamazungulira mukusintha ndi m'machitidwe osiyanasiyana, umaonetsa ubwino ndi chisangalalo cha moyo. Ngakhale kuti moyo wake uli m'mavuto ndi mu zophinja, samadandaula mokwiya, munthu otereyu safuna kuti moyo wake uthe mofulumira, samadandaula kapena kunyasidwa, ponena kuti "Kalanga ine! Dzuwa silinalowe" kapena "Ukadalibe usiku."

Indedi funsa munthu amene ali wachuma ndi wosatakataka ongotsamila pa zosangalatsa. "Ulibwanji?" umayembekezela kumva yankho lokhumudwitsa. "Nthawi sikupita konse, tiyeni tipange masewero a anthu awiri. Kapena apo tiyeni tipeze chisangalalo chimene chingapangitse nthawi kudutsa." Apo ayi udzamva madandaulo kuchokera mu zokhumba za m'dziko; " Ine ndilibe zimenezo ngati ndikadangopanga chakuti kapena chakuti."

Ndipo Kenaka umufunse munthu amene ali m'mavuto kapena wa ntchito kapena osauka amene amafunsidwa kuti "ulibwanji?" Ngati ali wanzeru adzayankha kuti; "mayamiko onse apite kwa Allah, zikuyenda". Ngati usiku sungabwere mofulumira ndikadamaliza ntchitoyi! Nthawi imadutsa mofulumira chimodzimodzinso moyo umadutsa mwachangu. Kunena zoona zinthu ndizovuta kwa ine, koma nazonso zidzatha." Chilichonse chimatha mofulumira, mokhudzidwa amanena kufunika kwa moyo, kudzera mu zikhomo ndi ntchito. Kumaphweka ndi moyo wa nthanzi, amapanga moyo kukhala owawa ndi kukhala ndi chiyembekezo chimodzi pakutha kwake mofulumira.

M'bale wanga amene ukudwala! Dziwa kuti kusapezeka ndi chiyambi cha mavuto ndi zoipa ngakhalenso machimo, zidatsimikizidwa mwatsatanetsatane m'magawo ena a Risale-i Nur. Ngati m'mene kusapezeka ndi koipa. Kunyasidwa ngati kumangidwa zili pafupi ndi kusapezeka ndipo zimayambitsa kukhumudwa kwa machitidwe ndi kusintha zimapezeka ndipo zimapangitsa kupezekako kudziwika. Ndipo kupezeka nkwabwino kwambiri ndi kuwala.

Zoona zake zikutanthauza kuti kudwala kwako kudabwera pa iwe ngati mlendo ndikuchita ntchito zambiri monga ngati kuyeretsa moyo wako wopambana, kuulimbitsa ndi kuupanga kuti upitilire, kuchepetsa maganizo ena aumunthu

pa chilengedwe chako pothandiza kwa odwala ndi kuonetsa mayina ochuluka a *Sani-i Dhul Jalal*. *Inshaallah* adzagwira ntchito yake mofulumira ndi kuchoka ndipo adzanena kwa moyo wathanzi kuti; " Bwera ndipo khala m'malo mwanga mpaka kalekale ndipo gwira ntchito yako. Nyumba ino ndiyako, khala muno m'moyo wathanzi."

Machilitso a Makumi Awiri

O munthu odwala amene ukusakasaka machilitso amatenda ako! Kudwala kuli m'mitundu iwiri. Mtundu oyamba ndiko Kudwala kwenikweni ndipo kwina ndi kongoganizira. Kumbali yakudwala kwenikweni *Shafi-i Hakim-i Dhul Jalal* (Mchilitsi wa nzeru zonse ndi otamandika) adasunga mu famasi yake ya mphamvu ya dziko lapansi makhwala amatenda alionse. Tsono machilitso enawa amafunikira matenda ake ake. Iye adalenga mamkhawala anthenda iliyonse. Sikulakwa kutenga makhwala ndikugwilitsa ntchito kuti achize matenda, koma aliyense ayenera kudziwa kuti mphamvu yake ndi machilitso zimachokera kwa Allah wa mphamvu. Iye amapeleka machilitso monga momwe amapelekera mankhwala. Potsatila zonena za anthu aluso, dotolo amene amaopa Allah ndi mankhwala amphamvu. Popeza matenda ambiri amabwera chifukwa cha kusagwiritsa bwino ncthito, kusadziletsa, kuononga kulakwitsa ndi kusasamala. Dotolo wa chipembedzo adzapeleka malangizo ndi njira zoti zitsatilidwe zomwe zili zovomelezeka

m'malamulo. Adzakana kusagwiritsa ntchito bwino ndikuononga ndikupeleka chilimbikitso. Munthu odwala amakhala ndi chikhulupiliro m'malangizo ake komanso chilimbikitso chake ndipo matenda ake amachepa; zimabweretsa chisangalalo kwa iye m'malo mokhumudwa.

Tikabwera kumatenda ongoganizira, mankhwala ake a mphamvu kwambiri ndi kusawalabadira. Ngati uwalabadira kwambiri matendanso amakula. Ngati sikuwatengela amachepa ndipo amabalalika. Ngati mkwiyo wa njuchi ukula zimamuunjikiranso m'mutu koposa koma ngati munthu sazisamala zokha zimabalalika. Chimodzimodzinso ngati wina asamala kwambiri za kaulusi koyendayenda pa diso mu mdima ndi chiopsyezo chimabweretsa kwa munthu, chonchoso chimakula ndipo chimapangitsa munthu kuthawa mofulumira ngati wa misala. Koma pamene ngati munthu sasamala za ichi amangoona ngati kaulusi wamba kakang'ono osati njoka ayi, ndipo amamuseka amene akuchita nako mantha ndi kunyasidwa

Ngati kudandaula ndi kunamizila kudwala kukula zimasanduka zenizeni. Ndi matenda oopsya amene amakhudza misepha imene imagwira ntchito poganiza; anthu oterewa amapanga mapiri kuchokera ku zulu zazing'ono kwambiri ndipo makhalidwe awo amaonongedwa. Makamaka ngati akukumana ndi dotolo opanda chisoni

kapena opanda chilungamo, zimapitirira kukhudza kunamizila kwawo. Kwa anthu olemera amataya chuma chawo, kapenanso amataya kaganizidwe kabwino kapenanso moyo wa thanzi.

Machilitso a Makumi Awiri ndi Mphambu Imodzi

M'bale wanga odwala! Matenda ako amabwera ndi ululu wa kuthupi. Komabe wazungulilidwa m'chisangalalo cha uzimu chofunika chimene chidzachotse chotsatira chake. Ngati uli ndi bambo ako, mayi ako ndi abale ako onse ali ali pamodzi ndi iwe, chisangalalo cha chisoni chawo chimene udachiwala kuyambira uli mwana udzachikumbukira ndipo udzaonanso maonekedwe a chifundo amene udalandira ku umwana wako. Poonjezera apa ubale umakubisa chimene chidali cha chinsinsi ndi chobisika. Izinso zimayang'ana pa iwe ndi chikondi kudzera mukutengeka ndi matenda. Komanso pa izi, matenda ako aku thupi amachepetsedwa mukusafunika. Komanso wasanduka mbuye wa ambuye popeza amene umawathandiza mwansangala pano akukuthandiza iwe mwa chisoni pochepetsa matenda ako. Poonjezela apo wadzikopa wekha potsatira zilakolako ndi chisoni cha munthu mwa anthu ndikupeza anzako ambiri othandiza ndi achisoni chinanso walandira lamulo kuchokera mukudwala kwako kuti upumule kuchokera ku ntchito zolemetsa ndipo umapumula. Chachidziwikile,

pamaso pazisangalalo zosafunikirazi ululu wako wochepa ukhonza kukupangitsa kuthokonza m'malo modandaula.

Machilitso a Makumi awiri ndi Mphambu Ziwiri

O m'bale wanga amene ukudwala kwambiri ngati opuwala! Choyambilira ndikupatsa uthenga wabwino kuti kwa okhulupilira opuwala amatengedwa ngati madalitso. Kalekalero ndimamva izi kuchokera kwa munthu oyera mtima ndipo sindinadziwe chifukwa chake koma pano chifukwa chimodzi cha izi zinachitika kwa ine motere: Ndi cholinga chofuna kukhala mu umodzi wa *Janabi-i Haqq* ndi kupulumutsidwa kuzoopsya zikuluzikulu za mdziko muno ndikupeza chisangalalo, anthu a Allah adasankha kutsatira ndondomeko ziwiri.

Ndondomeko yoyamba; *Rabita-i Mevt* (Kuganizira za imfa), poganizira kuti dziko lapansi ndilosakhalitsa ndipo iwowa ali ngati alendo osakhalitsa amene anapatsidwa ntchito zoti agwire za m'moyo wosatha.

Ndondomeko ya chiwiri; kudzera mukusala zochitika zamuchipemebedzo ndi kukhala m'moyo osatakasuka amayesera kuupha mzimu olamula zoipa ndikupulumutsidwa ku zoipa zake ndimaganizo osochera. Ndipo iwe m'bale wanga amene wataya theka la moyo wako wa thanzi!

Popanda kusankha udapatsidwa malamulo aiwiriwa amene ali afupi ndi osavuta ndi chiyambi chachisangalalo. Kutanthauza kuti m'mene iwe ulili zimakuchenjeza za chisangalalo cha ka nthawi kochepa cha mdziko lino ndipo kuti munthu ndi osakhalitsa. Dziko silingakutayenso kapena iwe mwa kusamvera kutseka maso ako. Ndipo chachidziwikire mzimu olamulira zoipa sungakunyenge ndizilakolako zochepa ndi zilakolako za nyama zimene zili theka la munthu amapulumutsidwa mofulumira kumayesero a mzimu.

Kutanthauza kuti kudzera mu m'chikhulupirilo chenicheni mwa Allah ndi kumvera Iye komanso kudalira mwa Iye, munthu okhulupilira akhonza kupindula mu kanthawi kochepa kuchokera kumatenda akulu ngati opuwala amafanana ndi mayeselo akulu a anthu oyera ntima. Matenda akulu ngati amenewa amakhala opepuka kwambiri.

Machilitso a Makumi Awiri ndi Mphambu Zitatu

Omunthu odwala osasangalala amene uli wekha ndiponso mlendo! Ngakhale kuti kukhala kwako m'kwawekha ndi ukapolo mdziko lachilendo pamodzi ndikudwala kwako zikadayambitsa kukhunzika pa iwe m'mitima youma kwambiri ndi kukodola chifundo ndi chisoni, "kodi chikadalowa m'malo mwa Namalenga wako wachisoni chosatha? Popeza amazionetsera iye mwini kwa ife pa

mayambiliro ama sura onse a mu Qur'an ngati wa *Rahman-i Rahim* (chifundo ndi wachisoni) ndipo ndikuwala kwa chisoni chake kumapangitsa amayi onse kukhala ndi ana ndikufewa kodabwitsaku ndichionetsero chimodzi chachifundo chake nyengo iliyonse kuyika pa dziko lapansi zisangalalo. Moyo osatha wa ku paradiso pamodzi ndi zabwino zake zonse ndi chionetsero chimodzi chachifundo chake. Chachidziwikire ubale wako ndi Allah kudzera m'chikhulupiliro, kumuzindikila kwake ndi kumufunafuna iye kudzera mukusowa, zimayambira mukudwala kwako ndi kuphinjika kwakukhala kwako kwa wekhawekha mdziko lachilendo kudzabweretsa chifundo chake pa iwe mofulumira. Chimene chimakhala m'malo mwa chilichonse. Popeza alipo nthawi zonse ndipo amayang'ana iwe, chilichonse chako chilipo. Amene alidi okhaokha mdziko lachilendo ndi amene sadalumikizane ndi *Khaliq-i Rahim* kudzera mchikhulupiliro ndi kumvera, ndikusasamala zakufuna kwa ubale umenewu.

Machilitso Makumi Awiri ndi Mphambu Zinayi

O iwe munthu amene umayang'anira ana odwala kapena anthu okalamba! Pamanso pako zili ngati malonda ofunika amoyo umene uli nkudza. Peza malondawo kudzera muchisangalalo ndi kupanga zinthu mwatsopano. Zidakhazikitsidwa ndi anthu achoonadi kuti matenda a ana ali

ngati masewero olimbitsa thupi lawo lomwe liri lofewa, katemera komanso ngati kukonzekera kwakukulu kowachititsa kukhala amphamvu mtsogolo mukusintha kwa kukulu kwa mudziko. Mukuonjezera mu zitsanzo zochuluka za nzeru potengera moyo wamwana wa dziko lino. Mmalo mwa masautso amachimo mwa anthu akukulu akulu amene amayang'ana za moyo wa uzimu ndipo ndi njira yoyeretsera moyo. Matenda ali ngati katemera owonetsetsa kuti moyo wamwana wa mtsogolo wauzimu upitirile kapenanso moyo umene uli nkudza; ndizabwino zobwera kamba kamatenda amenewa zimapita ku buku la ntchito zabwino za makolo, makamaka za amayi amene kudzera muchisoni chachikulu amafuna nthanzi la mwana wake ndinso lake lomwe.

Kuyang'anira anthu okalamba kudakhazikitsidwa momveka bwino ndi zochitika zochuluka zokamba za mbiri zimene pamodzi umalandira mphoto yayikulu kwambiri. kulandira mapephero amunthu okalamba makamaka amakolo ndi kukondweretsa mitima yawo powatumikira mokhulupilika, iyi ndi njira yachisangalalo cha moyo uno ndi umene uli mkudza. Ndipo zidakhazikitsidwa kuti mwana wamwayi amene amamvera pa mbuyo pa ukalamba wa makolo ake nayenso ana ake adzamumvera chimodzimodzi. Ndipo ngati mwana watsoka samvera makolo ake adzalangidwa munjira zoopsya zosiyanasiyana

m'dziko lino komanso m'moyo umene uli nkudza. Indedi kuyang'anira anthu posatengera achibale ake okha amene ali okalamba kapena achichepele komanso onse amene ali okhulupilira, ngati wina wakumana nawo anthu oterewa popeza kudzera m'chikhulupiliro chachikulu muli ubale weniweni ndikwatumikira anthu odwala okalamba amene akusowekera chinthandizo. Ngati afunikira chinthandizo kwa amene ali ndi kuthekera kotero, nzofunikira mchisilamu.

Machilitso a Makumi Awiri ndi Mphambu Zisanu

Abale anga odwala! Ngati mukufuna kupindula kwa kukulu ndi chisangalaro chenicheni cha machilitso, kwezani chikhulupiliro chanu. Kutanthauza kuti kudzera mukulapa ndi kufunafuna chikhululuko ndi kuchita mapemphero asanu olamulidwa atsiku ndi tsiku, gwiritsani ntchito chikhulupiliro. Machilitso oyeletsedwa ndi mankhwala amene amachokera m'chikhulupiliro.

Ndithudi, chifukwa chokonda dziko lapansi ndi kukakamira ku ilo, ngati iwe uli ndi matenda akulu ngati dziko lapansi monga kusamvera.

Tatsimikiza m'magawo ambiri a mabuku a *Risale-i Nur* kuti chikhulupiliro chimachiza kamodzi kuthupi lako kwakukulu ngati m'mene dziko liliri, kumene kuli kuvulala kamba ka imfa ndi kulekana ndikuchipulumutsa kuchokera ku mabala ndikuwachilitsiratu.

Koma ndafupikitsa zokambazi choncho kuti musaopsyezedwe. Koma mankhwala a chikhulupiliro, amaonetsa mphamvu yake ukamachita mapemphero achipembedzo mwa kuthekera kulikonse. Kusamvera, makhalidwe oyipa ndi zilakolako za mzimu ndi zisangalalo za ka nthawi kochepa zimateteza kagwiridwe ka ntchito kake. Popeza kudwala kumachotsa kusamvera, kumadula zilakolako za zakudya ndi kutchinga ku zisangalalo za kanthawi kochepa choncho uchitenge ngati chinthu chofunikira. Gwilitsa ntchito mankhwala oyeretsedwa ndi kuwala kwa chikhulupiliro kudzera mu kulapa ndikufunafuna chikhululuko ndikuchita ma dua ndi mapemphero.

Janabi-i Haqq abwezeretse moyo wako wathanzi ndi kupanga kudwala kwako kukhala ngati malipiro amachimo ako. Ameen Ameen Ameen.

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ الَّذِی هَدٰینَا لِهٰذَا وَمَا كُنَّا

لِنَهْتَدِیَ لَوْلَآ اَنْ هَدٰینَا اللّٰهُ لَقَدْ جَآءَتْ رُسُلُ

رَبِّنَا بِالْحَقِّ

سُبْحَانَكَ لَا عِلْمَ لَنَآ اِلَّا مَا عَلَّمْتَنَآ اِنَّكَ اَنْتَ الْعَلِیْمُ الْحَكِیْمُ

اَللّٰهُمَّ صَلِّ عَلٰی سَیِّدِنَا مُحَمَّدٍ طِبِّ الْقُلُوْبِ

وَدَوَائِهَا وَعَافِيَةِ الْأَبْدَانِ وَشِفَائِهَا وَنُورِ
الْأَبْصَارِ وَضِيَائِهَا وَعَلٰى اٰلِهٖ وَصَحْبِهٖ وَسَلِّمْ

KALATA YA KHUMI NDI MPHAMBU
ZISANU NDI ZIWIRI

(Ikupezeka m'gawo limodzi mu buku lotchedwa, the twenty- fifth flash)

KALATA YACHIPEPESO PA IMFA YA MWANA

"Ndipo mdzina lake alemekezeke."

بِاسْمِهٖ وَ اِنْ مِنْ شَيْءٍ اِلَّا يُسَبِّحُ بِحَمْدِهٖ

Ndipo chilichonse chimamulemekeza ndi kumutamanda.

O m'bale wanga wa m'moyo uli mkudza, Hafiz Halid Efendi!

Mdzina la Allah wachifundo chambiri wa chisoni.

بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

وَبَشِّرِ الصَّابِرِيْنَ ۝ اَلَّذِيْنَ اِذَآ اَصَابَتْهُمْ مُّصِيْبَةٌ

قَالُوْٓا اِنَّا لِلّٰهِ وَاِنَّآ اِلَيْهِ رَاجِعُوْنَ

"Ndikupeleka uthenga wabwino kwa odwala amene panthawi yomwe amaphinjika ndi masautso

amati اَلْحُكْمُ لِلّٰهِ *Tidachokera kwa* ***Janabi Haqq*** *ndipo ndi kwa Iye tidzabwelera."*

M'bale wanga. Imfa ya mwana wako yandikhumudwitsa koma اَلْحُكْمُ لِلّٰهِ (lamulo ndi la Allah) kukhutitsidwa ndi lamulo lalikulu ndi kudzipeleka kwakukulu ndi chizindikiro cha chisilam ndi kupempha Allah wa mphamvu zonse akupatse mtima opilira ndipo amapanga omwalilayo kukhala okuthandizira m'moyo umene uli nkudza.

Ndifotokoza mfundo zisanu zomwe zili uthenga weni weni wabwino ndi kupeleka chithokozo cheni cheni kwa iwe ndi anthu ena okhulupilira mchoonadi ngati iwe.

Mfundo yoyamba

Tanthauzo la mawu oti وِلْدَانٌ مُخَلَّدُونَ

(Achinyamata amuyaya) m'buku lanzeru la Qur'an-i Hakim lili ndi mau awa. Vesili limaonetsa ndi kupeleka uthenga wabwino oti ana a athu okhulupilira amene amamwalira asanafike nsinkhu okhwima adzakhalabe amuyaya, ana okondedwa oyenera paradiso: Ndipo kuti adzakhala njira yachisangalaro chosatha kuwalandira makolo awo amene adafika ku paradiso ndipo kutiadzakhala

njira yotsimikizira makolo awo. Chisangalaro chokometsetsa ngati kukonda ndi kusamala ana, kuti zinthu zonse zosangalatsa zidzapezeka ku paradiso. Choncho kuti mayankhulidwe anthu amene amanena kuti popeza paradiso simalo obelekanirana, sikudzakhala chikondi ndi chisamaliro cha ana siolondola. Ndipo kuti kupeza zaka zikwi zikwi zoyela, chikondi chopanda ululu ndi kusamalira وِلْدَانٌ مُخَلَّدُونَ (ana amuyaya) m'malo akanthawi kochepa ngati zaka khumi zokonda ana zosakanikirana ndi chisoni m'dziko muno ndi chiyambi chenicheni cha chisangalaro cha anthu okhulupilira.

Mfundo ya chiwiri

Mnthawi ina munthu adali mndende, adamutumizira m'modzi mwa ana ake okondedwa. Munthu wa m'ndende adavutika ndi chosoni chake chomwe, popeza sakadatha kumusangalatsa mwanayo choncho adamvanso chisoni pa zovuta zake. Kenaka olamura wachisoni adamutumizira munthu uja uthenga womwe umati "chachidziwikire mwana uyu siwako ndi wanga ndiwa anthu anga. Ndidzamutenga ndikumusamalira kumalo abwino." Kenaka munthu uja adali ndi mkwiyo ndipo adati "Sindidzakupatsani mwana wanga amene alichipepeso changa."

Ndipo anzake adati kwa iye; “kudandaula kwako kulibe tanthauzo.”

Ngati mwana amene ukumumvera chisoniyu adzapita ku malo opambana ndi achisangalaro m’malo mwa malo oipa ngati ano, onunkha ndi malo odetsa nkhawa. Ngati ukudzimvera chisoni wekha ndikufunafuna zabwino zaiwe mwini, ngati mwana akhalabe kuno, udzavutika kwambiri ndi khawa ndi ululu pazovuta za mwana wakoyo poonjezera chikaiko chako, zabwino zako za nthawi yochepa.

Ngati adzapite kumeneko udzakhala mwayi wako waukulu poti chidzakhala chiyambi chopezera chifundo cha mfumu ndipo adzakhala akuthandizira.

Mfumu idzapanga kuti ikumane nawe. Akunenetsa kuti sadzamutumiza kundende kuti ungamuoneso, adzakutulutsa iwe mndende ndikukuitana ku nyumba ya chifumu ndipo adzakulola kukumana ndi mwana wako kumeneko, ngati uli ndi chikhulupiriro mwa mfumu ndikumuvera.

M’bale wanga okondedwa ngati fanizoli ukuyenera kuganiza motere, ngati anthu ena okhulupilira pamene ana awo amwalira. Mwanayo adali osalakwa ndipo Mulengi wake ndi Allah wachisoni chonse ndi owolowa manja.

Wamutengera iye ku chisomo chake chabwino ndi chifundo m’malo mwa kumulera ndi chisoni

changa choperewela. Wamutulutsa mchisoni, mmavuto, mndende yovuta ya dziko lino lapansi ndikumutumiza ku *Jannatul Firdaus* (minda ya ku paradiso.) Ndikosangalatsa bwanji kwa mwana. Ngati akadakhala mdziko lino la pansi, ndani amene akudziwa za mmene akadakhalira. Choncho sindingamuvere chisoni ndikudziwa kuti ndiwa mwayi. Pangotsala zopindulitsa kwa ine mwini ndipo sindimazivera chisoni pa zimenezo.

Ndipo sindimadandaula ndikukhala wachisoni. Popeza akakhalabe pa dziko pano akadapatsidwa zaka khumi za chikondi cha mwana cha kanthawi kochepa chosakanikirana ndimaululu. Ngati akadakhala wa ngwiro ndipo akadakwanitsa zinthu za m'dziko lapansi mwina kutheka akadandithandiza. Koma kamba ka imfa yake wakhala ngati nkhala pakati amene ali njira ya zaka zochuluka za chikondi cha mwana ku paradiso wa muyaya ndikuchisangalalo chosantha. Kawiri kawiri, munthu amene amataya chikaiko, nthawi yomweyo amapeza mphindu ndikupeza zochuluka, zopindula za mtsogolo sizionetsa kudandaula ndi chisoni, salira mukulekanaku.

Mfundo ya Chitatu

Mwana amene adamwalira adali cholengedwa, cholamulidwa, kapolo kuphatikizapo zonse zomwe adalinazo. Chopangidwa cha *Khaliq-i Rahim* ndipo ndi chake, adali nzawo wa makolo ake, ndipo

adamuika mongoyembekezera pansi pa ulamuliro wawo.

Allah adapanga mayi ndi bambo kukhala otumikira mwana. Powabwenzera pa ntchito yawo Allah adawapatsa chisoni cha chisangalalo ngati malipiro a pompo pompo. Pano ngati chofunika cha chifundo ndi nzeru, chimene *Khaliq-i Rahim*, amene amayang'anira mazana asanu ndi anayi ndi makumi asanu ndi anayi ndi mphambu zisanu ndi zinayi. Za zinthu chikwi cha za mwana, watenga mwana kuchokera kwa iwe ndikupangitsa ntchito yako kufika kumapeto ndi kulira modandaula ndi kulekana chifukwa cha kanthu kamodzi pa maso pa mwini wake weniweni wagawo lalikulu mu njira yomwe imabweretsa kudandaula zomwe sizimamuyenera munthu okhulupirira koma makamaka zimawayenera anthu onyalanyaza ndi osochera.

Mfundo ya Chinayi

Ngati dziko likadakhala la muyaya ndipo kuti munthu akadakhalamo wamuyaya ndipo kuti kulekana kukadakhala kwa muyaya kudandaula kwa chisoni ndi mavuto akulu akadakhala ndi tanthauzo. Koma popeza kuti dziko lino ndi nyumba ya alendo, kulikonse mwana wakufunayo wapita, iwe ngakhale ifenso tidzapita kumeneko, kuonjezera apa imfa imeneyi siyoyenera kwa iye, ndi njira yodutsilapo. Ndipo kuti kulekana sikwamuyaya mtsogolomu, m'manda ndinso

m'moyo umene uli nkudza adzakumana. Wina akuyenera kunena kuti اَلْحُكْمُ لِلّٰهِ lamulo ndi la Allah adamupeleka ndipo wamutenganso.

Akuyenera kunena kuti *Alhamdulillah ala kuli hal,* ndi kupeleka mayamiko mopilira.

Mfundo ya Chisanu

Chisoni, amene ali osamvetsetseka, wokongola kwambiri, wangwilizano ndi zionetsero zabwino za chifundo chachikulu ndimakhwala owala modabwitsa. Chimaposa chikondi chenicheni mofulumira chimakhala njira ya umodzi wa *Janabi Haqq*. Chikondi chozimbaitsa ndi chapadziko lapansi chimasanduka kukhala choonadi ndi mavuto aakulu ndi kupeza *Janabi Haqq*, koma chisoni chimalumikiza mtima kwa Allah moyandikana, mwa ubwino ndimopanda chovuta chilichonse. Bambo ndi mayi onse amakonda mwana kuposa dziko lapansi. Pamene mwa wawo watengedwa pakati pawo ngati ali a mwayi ndi okhulupilira mwa choonadi, kumasintha nkhope zawo kuchokera pa dziko pano ndikupeza weniweni opeleka chisangalaro.

Zimanenedwa kuti "Popeza dziko lapansi ndi losakhalitsa sikoyenera kuti mtima zizikakamira za mdziko lapansi kulikonse kumene mwana wapita, munthu amapanga zokhudzana ndi malowo, izi

zimamupangitsa kupeza moyo wapamwamba wauzimu.

Anthu onyalanyaza ndi osochera amachepetseledwa chisangalaro ndi uthenga wabwino wa mfundo zisanuzi.

Mukhoza kuona m'men mnyengo zawo ziliri zomvetsa chisoni motere, amaona mwana wawo yekhayo mkatikati mwa mavuto a imfa ndipo chifukwa cha maganizidwe awo dziko kukhala lamuyaya ngati chotsatila cha kusamvera ndi kusochera kwao, amaganiza kuti palibe imfa kapenaso kulekanaso kwamuyaya. Amaganizira za iye mdziko la m'manda ake ogona a wofuwofu ndipo chifukwa cha kusamvera kapena kusochera, saganizanso za paradiso ya chifundo ndi kumwamba kwa zabwino za wa chifundo wa chifundo chonse, mukhoza kuona fanizo ndichimene chimalekanitsa chisoni ndi kudandaula kumene amavutika nako. Pamene chikhulupiliro ndi chisilamu chimati kwa okhulupilira, *Khaliq-i Rahim* (Mlengi wake wa chisoni chonse) adzatenga mwana ameneyu amene ali m'mavuto a imfa kuchokera mdziko Lapansi ndi kupita naye ku paradiso.

Adzampanga iyeyo ngati mkhala pakati wako ndi mwana wa chisangalaro chosatha. Msiyanowo ndi wakanthawi kochepa, usadandaule nako ndipo nena kuti, mwini ulamuliro ndi Allah. Kwa Allah

ndikomwe tidachokera ndipo kwa Allah ndikomwe tidzabwelere.

اَلْحُكْمُ لِلّٰهِ ۞ اِنَّا لِلّٰهِ وَاِنَّآ اِلَيْهِ رَاجِعُونَ

اَلْبَاقِي هُوَ الْبَاقِي

Said Nursi